

A Bereya

CHRISTADELPHIAN

Vol 021



**Thupi la Khristu ku Africa ndi padziko lonse
lapansi liyenera kukhala thupi lomwe
limayang'ana kwambiri kuunikiridwa ndi
chilimbikitso m'malemba.**



SEPTEMBER, 2026

**...analandira mawu ndi mtima wonse, ndipo
anafufuza m'malemba tsiku ndi tsiku, ngati
zinthuzo zinali choncho."**

KHRISTU AKUBWERA POSACHEDWAPA NDIPO ADZALAMULIRA PADZIKO LAPANSI--

A photograph of a field of daisies with yellow centers and white petals, growing among tall green grass. The scene is reflected in a body of water in the foreground, creating a symmetrical effect. The lighting is warm, suggesting late afternoon or early morning.

Zotsatira za Galasi

Pamene ndikudziyang'ana mu galasi, kodi ndimaona chiyani? Kodi ndimadzikwiya? Kapena ndimadzinyada? Kodi ndimamva bwanji za zimene ndachita bwino? Kodi ndimakonda nsidze zanga? Tsitsi langa? N'chiyani chimene ndingachite kuti ndikhale bwinoko?

Nthawi zina ndimadzinyoza chifukwa cha zoyipa ndi zosayenera zimene ndikuziona. Nthawi zina ndimadzitamandira ndi kudzilimbikitsa.

Ngati ndikuoneka wonyansa mu galasi, mkati mwanga ndimadziwa kuti ndikuoneka wonyansa, ndipo ndikhoza kuiona izo. Ndipo anthu enaso adzaiona. Kwa ena, kuoneka wonyansa kungakhale kwachizolowezi, ndipo ndingakumane ndi anthu ooneka woyipirapo kunja uko. Koma galasi silinalipo chifukwa cha zovala zokha. Monga Yehova ananenera Samueli pamene anabwera kudzadzoza mfumu, "munthu amayang'ana zooneka pamaso, koma Yehova amayang'ana mtima" (1 Samueli 16:7). Chilichonse chimene ndikuona mu galasi, Iye amaona kuposera pamenepo.

Ngakhale kuphunzira Baibulo kumatiwongolera nthawi zonse pa zimene tiyenera kuchita, kukhala nazo pa moyo kungakhale kovuta kuposa malingaliro a sayansi ya fiziki akagwiritsidwa ntchito pa moyo weniweni — kumafuna kuposa kungodziwa bwinolomwe.

Kudziyesa nokha n’kophweka, koma kuyenda bwino m’dziko limene anthu ena osadera nkhwaza zauzimu zako angathe kusokoneza zisankho zako mosavuta, kumafuna kuyenda mosamala kwambiri. Njira yotetezeka kwambiri kwa ine ndiyo kudzichotsera ndekha kwa anthu, kumene udindo wanga sungafike kupitirira ine mwini, ndipo ngati udindowo ungafikebe, ndiyenera kukhala wokonzeka kulandira zotsatira zake, ngakhale zikhale zoyipa motani, ndikudziwa bwino zomwe zikuchitika. Ndi lingaliro lomveka bwino, koma silo limene Malemba amatisiyira nalo. "Tisasiye kusonkhana pamodzi monga ena akuchitira, koma tilimbikitsane; makamaka pamene mukuona tsiku lija likuyandikira" (Ahebrei 10:25). Kudzichotsera kwa anthu kungamveke ngati kotetezeka, koma sikunaperekedwepo kwa ife ngati njira yomaliza.

Ndili paulendo umene ndikudzilowetsa modziwa m’magulu osiyanasiyana a anthu ndikulola anthu ambiri kulowa m’moyo wanga, ndikukhulupirira ndi kuyembekezera kuti alinsu ndi chiyembekezo ndi chikhulupiro chimodzimodzi ndi changa. Ndikuphunziranso kuti anthu osiyanasiyana ali ndi mphamvu yosiyana ya galasi. Ena alibe ngakhale magalasi ndipo amadalira munthu wina kuti awafotokozere za maonekedwe awo, ngati ali ndi nkhwaza ya maonekedwe kapena akufuna maganizo achiwiri. Ena adzakuonani muli ndi vuto la zovala koma sadzanena kanthu.

Kukula kwa uzimu sikungakhale ndi zizindikiro zoyezeka pa dziko lakuthupi. Mwatsoka, tingadziwe pokha pamene Khristu adzabwera kumene tili poyerekeza ndi ulemero wake. Ngati ndidalira abale kuti andisonyeze mmene ndililimo, ndikhoza kusocheretsedwa, kapena ine ndingasocheretse iwo. Chachiwiri n’chosachitika mosavuta, chifukwa cha malingaliro anga a "kusalowerera nawo" mpaka nditaona kuti n’kofunika.

Ndikanangokhala kundiyang’anira dziko likudutsa chifukwa cha zikhulupiro zanga ndiponso zochitika zoyipa zimene ndinakumana nazo pamene ndinali wodzipereka. Koma magazini angapo m’mbuyomo, nkhanu ya Mbale Sid inanena za kuyanjana ndi anthu ndi mmene kuyankhula kumathandizira. Izi zikuphatikizapo kutha kuyankhula za zoyipa ndi chidwi chomwecho monga zabwino. Zinamveka ngati kudziyesa, koma pamlingo waukulu kwambiri — kuyankhula zinthu m’mawu kumathandiza. Mwina vuto langa la zovala n’chifukwa choti ndadzipweteka ndipo sindikhoza kumanga bwino mabatani. Munthu wina ayenera kundithandiza.

Ndinganenenso kuti alipo anthu kunja uko amene sanayang’anepo, ndipo sadzayang’anapo, mu galasi.

Pa Loweruka lililonse ndimadzipangira lipoti pa ine ndekha, mongomang’amba. Kodi ndikuganiza kuti Mulungu wandikondwera nane kwambiri kapena pang’ono sabata ino? Ngati Khristu abwera, kodi angandikondwere? Yankho lakelo silikhudza za kukondweretsa wina aliyense sabata ino, koma za kukonzekera tsiku lenilenilo: "Okondedwa, tsopano ndife ana a Mulungu, ndipo sichinaoneke chimene tidzakhala. Koma tikudziwa kuti Yesu akadzaonekera, tidzafanana naye, pakuti tidzamuona Iyeyo monga momwe alili. Aliyense amene ali ndi chiyembekezo ichi mwa Iye adziyeretse yekha, monga Iye ali woyera" (1 Yohane 3:2–3).

Galasi, pomalizira pake, silinalipo kuti tizitamandira kapena kutsutsa chithunzi chimene tikuonacho. Lilipo kuti tiyeretsedwe.

matt 3:13-17

13 Nthawi imeneyo Yesu anachoka ku Galileya napita ku Yordani kwa Yohane, kuti akabatizidwe naye. 14 Koma Yohane anafuna kumuletsa, nati, “Ndiyenera kubatizidwa ndi Inu, ndipo Inu mukubwera kwa ine?”

15 Koma Yesu anayankha nati kwa iye, “Lolani kutero tsopano, pakuti ndi koyenera kwa ife kukwaniritsa chilungamo chonse.” Ndipo pamenepo anamulola.

16 Yesu atabatizidwa, anatuluka msangamsanga m’madzi; ndipo taonani, kumwamba kunatsegulidwa kwa iye, ndipo anaona Mzimu wa Mulungu ukutsika ngati nkhunda nukhala pa iye. 17 Ndipo mwadzidzidzi mawu anamveka kuchokera kumwamba, akuti, “Uyu ndi Mwana wanga wokondedwa, amene ndikondwera naye kwambiri.”

Ndemanga:

Yohane ankaitana anthu kuti alape, nawabatiza, poonetsa kuti iye sanali Khristu, koma kuti wina wamphamvu kuposa iye anali kubwera. Mateyu akutiiza kuti Yesu atafika kwa Yohane kuti akabatizidwe, Yohane anayesa kumuletsa, nati, “Ndiyenera kubatizidwa ndi Inu, ndipo Inu mukubwera kwa ine?” Yesu anayankha ndi mawu awa, “Lolani kutero tsopano, pakuti ndi koyenera kwa ife kukwaniritsa chilungamo chonse.”

Baibulo limaphunzitsa kuti ubatizo umodzi ndi wofunika pa chipulumutso. Nikodemo anaphunzira usiku umene anacheza ndi Yesu kuti ngati munthu sabadwanso mwa Mzimu ndi madzi, sangathe kuona ufumu wa Mulungu.

Yohane 3:1-3

1 Panali munthu wa Afarisi, dzina lake Nikodemo, mtsogoleri wa Ayuda. 2 Uyu anadza kwa Yesu usiku, nati kwa Iye, “*Aphunzitsi, tikudziwa kuti Inu ndinu mphunzitsi wochokera kwa Mulungu; pakuti palibe munthu angathe kuchita zizindikiro zimenezi mumachita Inu, Mulungu asanakhale naye.*” 3 Yesu anayankha nati kwa iye, “*Ndithu, ndithu, ndikuuza Iwe, Munthu akapanda kubadwanso, sangathe kuona ufumu wa Mulungu.*”

**Mbale Stephen
David**

Mpingo wa Berean ku Africa

Nkhani & Zochitika

A' Bereya Christadelphian

Africa

Kusonkhana Pachaka

Malo Madowa, Uganda

Masiku: 17-20 Disembala, 2026

Mutu: Khalani Inu Osandulika

Ndi chisangalalo kulengeza za ubatizo wa mbale Adam Julius (mpingo wa Mtondia), womwe unachitika pa 9 Ogasiti 2026, pa nthawi ya kafukufuku wa Baibulo wa Kitui weekend.

Tikupemphera kuti Atate wathu wakumwamba amutsogolere pa njira yopapatiza yomwe imatsogolera ku ufumu wosatha!



SEP
2026



bereanchristadelphian.africa

Kukula Kwa Chikhulupiriro, Kukula Kwa Chakudya: Munda Wathu Wa Keyhole ku Ikutha

Kuyambira pachiyambi, Mulungu anapatsa munthu munda kuti awusamalire, kuphatikiza ntchito ya thupi ndi cholinga chauzimu. Banja lathu ku Ikutha lavomera ntchito imeneyi mwa kumanga munda wa keyhole: bedi lozungulira, lokwezedwa, lomangidwa mozungulira dengu lapakati la feteleza wachilengedwe (compost), lingaliro lochokera kwa Mlongo Eileen.

Chifukwa Chimene Tinamangira

Timakhulupirira kuti umoyo wa tsogolo la anthu sudalira chakudya chosinthidwa cha m'masitolo, koma chimene ife tokha timaweta ndi kulima.

Kumanga Popanda Miyala

Miyala inali yosapezeka, choncho tinagwiritsa ntchito njerwa za bizinesi ya mbale wathu yopanga njerwa, tikuzimanga ndi dothi ndi madzi m'malo mwa simenti. Bulu wa mlongo wathu ankanyamula madzi ndi ngolo kuchokera kumtsinje wakutali. Tinasanjikiza bedi ndi zibade za chimanga, zinyalala za nyama, kenako dothi, ndipo tinadzala.

Mbewu Ndi Kukula

Zitsamba zinachokera ku msika wa Nairobi, mbande kwathuko, ndipo mbewu zinachokera ku East Africa Seeds ndi Simlaw Seeds pa mtengo wabwino. Mbewu iliyonse inamera kupatula thyme, phunziro, osati kulephera.

Banja Losinthika

Banja linapindula ndi masamba atsopano ndi luso la zakudya, pamene Mlongo Ivykaye ankaphunzitsa kuphika zomwe amalima ndipo anatenga mbewu kupita nazo ku minda yake ku Uganda. Router ya Safaricom 5G tsopano ikuwathandiza kufufuza, ndipo chidwi cha minda ya keyhole chikufalikira m'deralo.


Zovuta Ndi Zoyembekezera

Mbalame zinaononga zomwe zimakonda monga masamba a maungu, choncho malo odyetsera tsopano akuzikopa kutali. Zitsa za cassava zochokera ku Bungoma ndi zakudya za mbuyu (baobab) zawonjezera zokolola. Mvula isanayambe, tikufuna maukonde ndi ma router ambiri kwa mabanja oyandikana nawo, munda uliwonse ukusonyeza kuti kusamalira nthaka ndi mzimu ndi ntchito imodzi.

Chonde tumizani mauthenga achipembedzo aku Africa ku:

Gulu Lolemba la A' Bereya Christadelphian, ku Africa

Otembenuzidwa ndi
Mlongo Ruth Mkandawire
nnalolile@bereanchristadelphian.africa



Zipitirira mwezi wamawa Ambuye akalola---
